-Anthu onse anachokera kwa Adamu ndi Hava.

-Satana amkaganiza kuti angathe kumuwononga Mulungu pamuwononga Adamu ndi Hava.

-Koma Mulungu analonjeza zomutumiza Mpulumutsi amene adzamugonjetse Satana.



PHUNZIRO LA 12

1. Satana atafika kuti amunamize Hava, kodi anazibisa bwanji?
-Anabisala mwa njoka.

2. Kodi chifukwa chiyani Satana anaganizo zomunamiza Hava?
-Chifukwa chakuti Satana samkamukonda Hava.
-Chifukwa chakuti Satana amkafuna kumuwononga Hava.

3. Kodi Satana amayesa kufuna kuŵakodwetsa ndi kumaŵanamiza anthu masiku ano?
-Inde.

4. Kodi Satana amayesa bwanji pofuna kuŵakodwetsa ndi kuŵanamiza anthu masiku ano?
-Choyamba, Satana amalamkhula ndi ife m'maganizo athu.
-Kachiŵiri, Satana amalamkhula ndi ife kudzera mwa anthu ena.
-Kachitatu, Satana amalamkhula ndi ife kudzera mu ziwanda.

5. Kodi Hava anadziŵa kuti amkalankhulana ndi Satana?
-Iyayi.

6. Kodi Mulungu anamuwuza Adamu kuti chidzaŵawonekera chiyani akadzadya chipatso kuchokera mu Mtengo Wodziwitsa zabwino ndi Zoyipa?
-Iwo adzafa.

7. Kodi nanga Satana anamuwuza Adamu kuti chidzaŵawonekera chiyani akadzadya chipatso kuchokera mu Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa?
-Iwo sadzafa.
-Iwo adzafanana ndi Mulungu.

8. Kodi Satana amkamutcha Mulungu kuti ndi wotani?
-Wabodza.

9. Adamu ndi Hava atachimwa ndi kuzindikira kuti anali maliseche, kodi anapanga chiyani?
-Anazisokera wokha zovala za masamba.

10. Adamu ndi Hava atachimwa, anamva mtswatswa wa Mulungu akuyenda kubwera kudzaŵawona, kodi iwo anachita chiyani?
-Anambisala Mulungu.

11. Kodi ndi kotheka kumbisala Mulungu?
-Iyayi, Mulungu ali paliponse.

12. Kodi Satana amamuda ndani?
-Mulungu ndi anthu onse.

13. Kodi Satana amafuna kuti inu mudzimvera Mawu a Mulungu?
-Iyayi.

14. Kodi chifukwa chiyani Satana safuna kuti inu mudzimvera Mawu a Mulungu?
-Chifukwa chakuti Satana amaŵada anthu onse, ndipo amafuna kuti iwo apite ku Nyanja ya Moto Wosatha.

-Kodi Mulungu anachita chiyani pamene Adamu ndi Hava sanamumvere Iye?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 3:9

9-Ndipo Yehova Mulungu anaitana mwamunayo nati kwa iye, “Uli kuti?”

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamuyitana Adamu?



-Apa pali chitsanzo:

-Munthu amene akufuna kufa ndi matenda akubwera ku nyumba kwanu.
-Inu mukumugulira mankwala ndi chakudya odwalayo.
-Odwalayo akukhala ndi inu ku nyumba kwanu kwa masiku ambiri.

-Kenako, adwalayo akuchila.
-Munthuyo asanapite kwawo, akukuberani inu ng’ombe kenako ndikumapita.

-Tsiku lina, munthuyo akubweraso kwa inu atayambiranso kudwala kuja.
-Inu mukumulandiranso ndi kumamugulira mankwala ndi zakudya.
-Munthuyo ndikuchiranso.

-Munthuyo anakuberani inu ng’ombe, ndipo amayenera kulandira chilango.
-Koma inu mwamuthandizanso munthuyo.

-Kusamvera kwa Adamu ndi Hava, kumayenera kulandira imfa.
-Koma Mulungu analonjeza zotumiza Mpulumutsi kudzaŵapulumutsa iwowo.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 3:20

20-Adamu anamutcha mkazi wake dzina lakuti Hava chifukwa chakuti anali mayi wa anthu onse.

-Hava anali mkazi oyamba, ndipo ndi mayi wa anthu onse.
-Adamu anali mamuna oyamba, ndipo ndi bambo wa anthu onse.

-Satana adzamupweteka Mpulumutsi koma mapeto ake, Mpulumutsiyo adzamupweteka Satana.

-Mpulumutsi adzabwera kudzaŵapulumutsa anthu.

-Mpulumutsi adzabwera kudzaŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya tchimo.
-Mpulumutsi adzabwera kudzaŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya imfa.
-Mpulumutsi adzabwera kudzaŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya Satana.

-Mpulumutsi adzakhala mwana wa mamuna wa mnamwali.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu analonjeza zotumiza Mpulumutsi?
-Chifukwa chakuti Mulungu amaŵakonda kwambiri anthu onse.

-Kodi Adamu ndi Hava anali oyenera kulandira chikondi cha Mulungu?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani Adamu ndi Hava sanali oyenera kulandira chikondi cha Mulungu?
-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava sanamumvere Mulungu koma Satana.

-Kodi kusamvera kwa Adamu ndi Hava kumayenera kulandira chiyani?
-Kusamvera kwawo kumayenera kulandira imfa yosatha.

-Kusamvera kwa Adamu ndi Hava kunalandira imfa.
-Koma Mulungu analonjeza zotumiza Mpulumutsi kudzaŵapulumutsa iwowo.



-Kodi Mulungu samkadziŵa kuti Adamu akubisala?

-Mulungu anadziŵa kuti adamu akubisala.
-Mulungu ali palipose.

-Mulungu amaziwona zinthu zonse.
-Palibe amene angabisale kwa Mulungu.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamuyitana Adamu?

-Mulungu amkafuna kuti Adamu abwere kwa Iye kuti alape machimo ake.

-Mulungu amkafuna kuti Adamu abwere kwa Iye ndi kuvomereza kuti sanamumvere Mulunguyo.

-Mulungu amkafuna kuti Adamu abwere kwa Iye ndi kuvomereza kuti anamumvera Satana.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anali oyenera kumuyitana Adamu?

-Chifukwa chakuti Iye ndi amene anamulenga Adamu.
-Chifukwa chakuti Adamu ndi wa Mulungu.
-Chifukwa chakuti Mulungu anamulenga Adamu kuti adzimumvera Mulunguyo.

-Chifukwa chiyani Mulungu ndi woyenera kuŵayitana anthu onse?

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene analenga anthu onse.
-Chifukwa chakuti anthu onse ndi a Mulungu.
-Chifukwa chakuti Mulungu anaŵalenga anthu onse kuti adzimumvera Mulunguyo.

-Mulungu sanasinthe.
-Mulungu akuyitanabe anthu lero lino.

-Kodi Mulungu akuŵayitana bwanji anthu lero lino?

-Mulungu akuŵayitanabe anthu lero lino kupitira mu zinthu zimene Iye anazilenga.

-Zolengedwa za Mulungu zikuwonetsa kuti kuli Mulungu, ndipo Mulungu ndi amene analenga zinthu zonse, ndipo Mulunguyo akufuna kuti ife tizimumvera.

-Mulungu amaŵayitananso athu kudzera mu Buku Lake.

-Buku la Mulungu ndi Uthenga wa Mulungu kwa inu.
-Buku la Mulungu kulankhula kwa Mulungu kwa inu.

-Kodi Adamu anati chiyani Mulungu atamuyitana iye?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 3:10

10-Adamu anayankha, "Ndakumvani mukuyenda m'mundamu, ndipo ndinawopa chifukwa chakuti ndinali maliseche; chomcho ndinabisala."

-Kodi chifukwa chiyani Adamu ndi Hava amamuwopa Mulungu?
-Chifukwa chakuti iwo sanamumvere Mulunguyo.

-Apa pali chitsanzo:

-Mwini munda atabwera m'munda mwake ndikumupeza wakuba akuba m'mundamo, kodi wakubayo angabisale?
-Inde.
-Adamu ndi Hava anabisala kwa Mulungu chifukwa chakuti anamulakwila ndipo sanamumvere  Muluguyo.



-Kodi zizindikiro zakuti Mulungu analitemberera dziko la pasi ndi zotani?
-Kuli minga ndi tchire lambiri.
-Kuli njala ndi kusefukira kwambiri kwa madzi.

-Nyama zimaluma anthu.
-Anthu ayenera kugwira ntchito molimbikira kuti apeze zakudya.
-Anthu amadwala.
-Anthu amafa.

-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava sanamumvere Mulungu, dziko la pasi linatemberereredwa.

-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava sanamumvere Mulungu, anthu onse amafa.

-Chilango cha Mulungu pa kusamvera ndi imfa yosatha.
-Chilango cha Mulungu pa tchimo ndi imfa yosatha.

-Nthaŵi yomweyo, Mulungu atatha kupereka chilango kwa Adamu ndi Hava, kodi Iye analonjeza chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 3:15

15-Ambuye Mulungu anati, "Ndiyika udani pakati pa iwe ndi mkaziyu, padzakhala chidani pakati pa ana a mkaziyu ndi ana ako. Mwana wa Mkaziyu adzaphwanya mutu wako ndipo iwe udzaluma chidendeni chake."

-Nthaŵi yomweyo Mulungu atapereka chilango kwa Adamu ndi Hava, Iye anapereka lonjezo lakuti adzatumiza Mpulumutsi.

-Mpulumutsi adzabwera kudzalimbana ndi Satana.

-Kodi Mulungu anamulanga bwanji Hava?
-Hava adzidzamva kupweteka kwambiri pobereka.

-Chilango cha Mulungu kwa Hava ndi chilango cha Mulungu kwa akazi onse.
-Tsopano, akazi onse amamva kupweteka kwabiri akamabereka.

-Kachitatu, Mulungu anapereka chilango kwa Adamu.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 3:17-19

17-Ambuye Mulungu anati kwa Adamu, "Chifukwa chakuti iwe wamvera mkazi wako ndipo wadya chipatso chimene Ine ndinakulamura kuti usadye chija, mthaka idzakhala yotembereredwa chifukwa cha zimene wachitazi. Udzayenera kugwira ntchito ya thukuta nthaŵi ya moyo wako onse, kuti upeze chakudya chokwanira.
18 M'thakamo mudzamera zomera za minga ndi za nthula, ndipo iwe udzidzadya zomera za kuthengo.
19 Udzayenera kukhetsa thukuta kuti upeze chakudya, mpaka udzabwerera ku nthaka kumene unachokera. Unachokera ku dothi, udzabwereranso ku dothi komweko."

-Kodi Mulungu anamulanga bwanji Adamu?
-Adamu adzidzalima pa dothi ndi thukuta lambiri koma adzidzakolora zokolora za pang'ono.

-Chilango cha Mulungu kwa Adamu ndi chilango cha Mulungu kwa amuna onse.
-Tsopano, amuna onse amalima pa dothi ndi thukuta lambiri koma amakolora zokolora za pang'ono.

-Kodi Mulungu anamupatsanso Adamu chilango chotani?
-Mulungu analitemberera dziko lonse la pasi.



-Kodi Mulungu anati chiyani kwa Adamu?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 3:11

11-Ndipo Ambuye Mulungu anati, "Kodi ndi ndani amene wakuwuza kuti uli maliseche? Kodi wadya chipatso kuchokera mu Mtengo umene ndinakulamula kuti usadye uja?"

-Kodi Mulungu anadziwa kuti Adamu wadya chipatso?
-Inde.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu anamufunsa Adamu kuti ngati wadya chipatso?

-Mulungu amkafuna kuti Adamu abwere kwa Iye ndi kulapa tchimo lake.

-Mulungu amkafuna kuti Adamu abwere kwa Iye ndi kuvomereza kuti sanamumvere Mulunguyo.

-Mulungu amkafuna kuti Adamu abwere kwa Iye ndi kuvomereza kuti wamumvera Satana.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu ndi amene anali oyenera kumufunsa Adamu?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anamulenga Adamu.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anaŵalenga anthu onse, Iye ndi amene ali oyenera kuwafunsa anthu onse.

-Tsiku lina, Mulungu adzaŵafunsa anthu onse, ndipo anthu onse adzamuyankha Mulunguyo.

-Kodi Adamu anayankha chiyani, Mulungu atamufunsa iye?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 3:12-13

12-Munthu uja anayankha, “Mkazi amene munandipatsa kuti adzikhala ndi ine uja, ndi amene anandipatsa ine chipatso cha mu mtengo muja, ndipo ndinadya.”
13-Kenako Ambuye Mulungu anamufunsa mkazi uja, “Kodi wachitazi, wachitiranji?”
Mkaziyo anati, “Njoka ndi imene inandinyenga kuti ndidye, ndipo ndinadya.”

-Adamu anamusambira m’manja Hava, ndipo Hava anayisambira m’manja njoka.

-Mulungu anali atazidziwa zowona zenizeni.
-Palibe chiwona chenicheni chimene chimabisika kwa Mulungu.

-Kodi munthu wina akagwidwa akuba, amachita chiyani?
-Amayesa kumusambira m’manja munthu wina.

-Tikhoza kuŵapusitsa anthu ena pomusambira m’manja munthu wina.
-Sitingathe kumupusitsa Mulungu pumusambira m’manja munthu wina.

-Nthaŵi zonse Mulungu amazidziwa zowona zenizeni.

-Nthaŵi zonse Mulungu amaŵapatsa chilango anthu amene samamumvera Iye.
-Nthaŵi zonse Mulungu amaŵapatsa chilango anthu amene amalakwa.
-Poyamba, Mulungu anapereka chilango kwa njokayo.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 3:14



14-Chomcho Ambuye Mulungu anati kwa njokayo, “Chifukwa chakuti wachita zimenezi,uli otembeleledwa kuposa nyama za mitundu yonse ya pa dziko la pasi pano, zoweta ndi za ntchile zomwe! Kuyambira lero mpaka kalekale udzikwawa ndi mimba yako, ndipo chakudya chako chidzikhala fumbi .”

-Kodi Mulungu anayilanga bwanji njoka?

-Ngati chilango, njoka iyenera kukwaŵa ndi mimba yake.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anapereka chilango kwa njoka?

-Njoka siyinalankhule kwa Hava.
-Satana yekha ndi amene analankhula kwa Hava.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu anapereka chilango kwa Njoka?

-Chifukwa chakuti Mulungu amapereka chilango pa tchimo lililonse.
-Chifukwa chakuti Satana anagwiritsa ntchito njoka pa tchimo.
-Mulungu amapereka chilango pa tchimo lililonse.

-Kachiŵiri, Mulungu anapereka chilango kwa Hava.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 3:16

16-Ambuye Mulungu anati kwa mkaziyo, “Ndidzawonjezera zovuta zako pamene udzakhala ndi pathupi , udzamva kuwawa pa nthaŵi imene udzidzabereka ana.Udzidzakhumbira mamuna wako, ndipo iye adzakulamulira iwe.”